# Malongosoledwe a coonadi ca m’Baibulo

## Za kufunafuna Mulungu

1. Mitima yathu ifuna Mulungu
2. Sitikhoza kuona Mulungu
3. Tikhoza kuona nchito za Mulungu
4. Mulungu analankhula kwa anthu a kale
5. Mulungu alankhula kwa ife
6. Mulungu anatuma Mwana wake

## 1. Mitima yathu ifuna Mulungu

*Funani Yehova popezaka Iye, itanani Iye pamene ali pafupi – Yesaya 55.6*

**Kuwerenga**
Salimo 105.1-4

**Malongosoledwe**
Buku iri litiphunzitsa za Mulungu. Litiphunzitsanso za anthu ndi zonse zimene zotizungulira zimene tiona. Koma litiphunzitsa makamaka za Mulungu.
Bukuli litiphunzitsa za Mulungu koposa pakuti anthu onse ayenera kudziwa Mulungu. Mulungu ali wofunikira kwambiri. Anatilenga; ndife ake. Dziko lonse lapansi ndi lake komanso dzuwa, mwezi ndi nyenyezi zambirimbiri zakuwala pamwamba pathu ndi zake. Izi zonse ndi za Mulungu. Kodi simuganiza kuti tiyenera kumdziwa Mulungu?
Munsi m'mitima yathu muli kamau komwe katiuza kuti Mulungu aliko ndiponso kuti tiyenera kumudziwa. Anthu ena samvera kamau ako; iwo safuna kudziwa Mulungu. Anthu ena amvera koma adzipangira milungu ao. Anthu anapanga milungu mogwiritsa nchito mitengo ndi miyala. Anthu ena anapempha dzuwa ndi nyenyezi ngati ndizo milungu. Koma milungu yotero siyakhoza konse kutiona, kutimvera kapena kutithandiza. Tifuna kudziwa Mulungu woona amene ationa, atimvera ndi kukhoza kutithandiza pamene timfunika.
Kodi munaona mwana wa khanda kukweza manja yake kwa mai wake? Mwana wa khanda afunika mai wake ndi kumufuna. Mai asamalira mwana wake. Mai wabwino asamalira ana ake onse. Ndife ana a Mulungu pakuti anatilenga: ndife ake. Ndipo tifunika Mulungu kutisamalira. Buku iri linalembedwa kuthandiza ana kupeza Mulungu, kumdziwa ndi kumkonda. Powerenga bukuli tidzakambirana za Mulungu: ukulu wake, ubwino wake, cikondi cake, cisamaliro cake, zimene afuna kuticitira ndi zina zambiri.
Kudziwa Mulungu ndi kofunikira koposa m'dziko lonse lapansi! Kudzatisangalatsa moonadi. Pamene timdziwa Mulungu, tidzamkonda, tidzamkhulupirira ndi kumumvera.

**Kukambirana**
1. Kodi tidziwa bwanji momwe Mulungu aliri?
2. Kodi mukumva bwanji za anthu amene apembedza milungu ina?
3. Cifukwa ciani tifunika Mulungu?
4. Kodi mumacita ciani kuti mudziwe Mulungu?
5. Cifukwa ciani Mulungu ndi Mwini wathu?
6. Kodi mwalandira Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wathu kuti inu mukhale mwana a Mulungu mwa Iye?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Inu ndinu Mulungu woona. Kulibe wina koma Inu nokha. Tikuyamikani kuti ndinu Mlengi wa zonse. Tithandizani kukudziwani, makamaka kudziwa ndi kulandira Yesu Kristu Mpulumutsi kuti tikhale ana anu osati mwacilengedwe cabe koma ana anu mwa Yesu Kristu. Tikupempherani m'dzina lake, Amen.

## 2. Sitikhoza kuona Mulungu

*Palibe munthu adzandiona Ine ndi kukhala ndi moyo – Eksodo 33.20b*

**Kuwerenga**
Salimo 104.1-13

**Malongosoledwe**
Kodi mufuna kuona Mulungu? Inde. Koma sitikhoza kuona Mulungu. Kulibe munthu amene anaona Mulungu.
Cifukwa ciani sitikhoza kuona Mulungu?
Sitikhoza kumuona pakuti Iye ndi mzimu. Sitikhoza kuona mzimu.
Kodi mzimu ndi ciani?
Cabwino, pamene Mulungu anakulengani, anakupatsani thupi ndi mzimu. Mzimu wanu ukhala m'thupi lanu. Mzimu wanu ndi inudi. Ndi mzimu wanu wokhala m'thupi lanu umene umvera pamene tiwerenga, ndi mzimu wanu umene uganiza ndi kukonda. Ndi mzimu wanu umene ukondwera ndi ukupangitsani kusekerera. Ndi mzimu wanu umene ukhala wacisoni nthawi zina ndi kukupangitsani kulira.
Kulibe munthu amene akhoza kuona mzimu wanu. Koma mukhoza kumva kuti ukhala moyo m'kati mwanu.
Tsono, Mulungu ndi mzimu cabe. Alibe thupi. Cifukwa cake sitikhoza kumuona. Koma aona, akumva ndi kukonda. Aona ndi kumva zambiri kuposa zimene ife tiona ndi kumva, ngakhale sitikhoza kumuona Mulungu.
Kulinso cifukwa cakuti sitiyenera kuona Mulungu. Mulungu ndi wa ulemerero konse. Ici citanthauza kuti Iye ndi woyera kwambiri ndi wakuwala kwambiri.
Baibulo litiuza za mwamuna wochedwa Mose. Mose anali bwenzi wa pa mtima wa Mulungu. Mulungu ankalankhula naye nthawi zambiri. Koma Mose sanaone konse Mulungu.
Tsiku lina Mose anati kwa Mulungu, 'Conde, ndionetseni ulemerero wanu'.
Mulungu anati kwa Mose, 'Palibe munthu adzandiona ndi kukhala ndi moyo. Koma ndidzakubisala m'mpata wa tanthwe ndipo kenaka ndidzakupitirira.'
Mose yekha anakwera phiri. Mulungu anamubisala pakati pa matanthwe ndipo Mulungu anampitirira. Mulungu anaonetsa pang'ono kwa ulemerero wake. Ngakhale mwamuna monga Mose sanakhoze kuona zambiri za ulemerero wa Mulungu koma pang'ono cabe.
Pamene Mose anatsika phiri, nkhope yake inawala monga dzuwa. Kuona pang'ono kwa ulemerero wa Mulungu kunasandutsa nkhope yake kuwala kotero kuti anthu anamuopa Mose.
Ulemerero wa Mulungu ndi wakuwala kotero kuti palibe munthu amene angalimbe mtima kumuona. Sitipirira kuyang'ana dzuwa pamene liwala. Kuyang'ana dzuwa kuwawitsa maso athu. Ulemerero wa Mulungu ndi wamkulu kuposa ulemerero wa dzuwa.
Ndi cabwino kuti sitikhoza kuona Mulungu.
Dzuwa ndi nyenyezi zitiuza ulemerero wa Mulungu. Koma ngati tiona Mulungu kapena kuona pang'ono kwa ulemerero wake, tidzamva mantha waukulu! Sitikhoza ngakhale kukhala ndi moyo!

**Kukambirana**
1. Kodi munthu akhoza kuona Mulungu?
2. Cifukwa ciani sitikhoza kuona Mulungu? Patsani zifukwa ziwiri.
3. Cifukwa ciani ndi cabwino kuti sitikhoza kuona Mulungu?
4. Kodi mukumva bwanji za ulemerero wa Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Ulemerero wanu ndi wamkulu kotero kuti sitikhoza kukuonani. Ndinu woyera ndi wolemekezeka. Ife ndife anthu ang'ono ndi ocimwa. Tithandizeni kukulemekezani ndi kukupembedzani moyenera. Tikupemphani m'dzina la Yesu, Mkhalapakati, Amen.

## 3. Tikhoza kuona nchito za Mulungu

*Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu – Salimo 19.1a*

**Kuwerenga**
Salimo 19.1-7

**Malongosoledwe**
Kuli zinthu zambiri zimene tikhoza kuona. Kuli zambiri zimene tingaphunzire.
Kodi mudziwa njira momwe tiphunzira?
Tiphunzira mwa kuona ndi kumva.
Kodi tingaphunzire ciani kuli Mulungu m'njira izo? Sitikhoza kumuona. Sitikhoza kumumvera kulankhula kwa ife. Ngati ziri tero, tingaphunzire bwanji za Mulungu kodi? Kodi timdziwe bwanji?
Tikhoza kumudziwa mwa zinthu zimene Iye analenga.
Kodi munaonako nyenyezi zakuwala pa thambo?
Kodi mumaona mwadzumwadzu pa dziko lapansi lalikulu? Kuli zinthu zambiri zodabwitsa pa dziko lapansi: nyama zabweya, mbalame, maluwa ndi tizirombo. Kuli nyanja zazikulu kwambiri ndipo nsomba zazikulu ndi zazing'ono ziri momwemo.
Kodi ndi yani amene analenga izi zonse? Kodi ndi yani amene amasamalira izi zonse? Zoona, kuyenera kukhala wolenga izi zonse. Wolengayo ndi Mulungu.
Nthawi zina tikumva mabingu ndi kuona mphezi. Inu ndi ine sitikhoza kupanga mabingu ndi mphezi. Sitikhoza kupanga mitambo ndi mvula. Sitikhoza kuyendetsa mphepo ndipo sitikhoza kuletsa mphepo pamene iomba. Izi zonse zimene sitikhoza, zitiuza kuti kuli Mulungu wamkulu. Iye apanga mabingu ndi mphezi. Apanga mphepo ndi mvula.
Nthawi zina tikumva mbalame yaing'ono kuimba. Sitikhoza kupangitsa mbalame kuimba nyimbo yabwino. Sitikhoza kuiphunzitsa kumanga fukwe lake laling'ono. Pamene tiona mbalame yaing'ono kutuluka ndi kuimva pamene iimba, tidziwa kuti kuli Mulungu wamkulu amene amalenga mbalame.
Maluwa aoneka bwino kwambiri. Ali ndi magawo ooneka bwino. Kuli maluwa a mitundu yosiyanasiyana: maluwa obiriwira, acikasu ndi ofiira. Maluwa ena asungiramo madzi abwino. Ena anunkhira bwino kwambiri. Yang'anani mosamalira maluwa ndipo onani cikomero cao. Ndipo ganizirani za mbeu zimene maluwa amabala. Sitikhoza kupanga maluwa m'modzi wamoyo wakusunga madzi abwino ndi wonunkhira bwino. Mulungu yekha akhoza. Ndiye maluwa atiuza kuti Mulungu aliko.
Tidziwa kuti Mulungu aliko cifukwa tikhoza kuona zimene anacita. Tiona zimene Iye analenga.

**Kukambirana**
1. Kodi tidziwa bwanji kuti Mulungu aliko?
2. Citanthauzanji kwa inu kuti Mulungu aliko?
3. Patsani zitsanzo zisanu za zimene Mulungu analenga.

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Inu ndinu Mlengi wa zonse. Masiku onse timaona nchito zanu zazikulu. Inu ndinu wamkulu ndithu. Ife ndife ang'ono ndipo nthawi zambiri tilephera kukulemekezani moyenera. Mutikhululukire ndi kutikonzera kuti miyoyo yathu ndi yodzala ndi ulemerero wanu. Tikupemphani m'dzina la Yesu Kristu Mpulumutsi, Amen.

## 4. Mulungu analankhula kwa anthu a kale

*Nenani, Yehova, popeza mnyamata wanu akumva – 1 Samueli 3.9b*

**Kuwerenga**
1 Samueli 3.1-10

**Malongosoledwe**
Adamu ndi Hava anali anthu oyamba ndithu amene Mulungu analenga: mwamuna ndi mkazi, iwo awiri cabe. Atalenga Adamu ndi Hava, Mulungu ankalankhula nao. M'madzulo pamene kunayamba kuda, Iye ankabwera ku munda kulankhula nao.
Zaka zambiri zitapita, Mulungu analankhula kwa mwamuna wochedwa Abrahamu. Abrahamu anali bwenzi la Mulungu.
Mulungu analankhulanso kwa Mose. Mulungu analankhula kwa Mose nthawi zambiri. Nthawi ina, Mose anali pamodzi ndi Mulungu pamwamba pa phiri la Sinai masiku makumi anai. Mose sanayenere kudya, pakuti Mulungu anamsamalira pamene analankhula kwa iye.
Baibulo litiuzanso momwe Mulungu analankhula kwa mnyamata usiku wina. Mnyamatayu ankakhala m'Kacisi ya Mulungu. Dzina lake ndi Samueli.
Samueli ankathandiza Eli, wansembe wokalamba, kusamalira Kacisi ya Mulungu. Usiku wina Mulungu analankhula kwa Samueli.
Samueli anali pa bedi. Mulungu anaitana, 'Samueli! Samueli!'
Samueli anaganiza kuti Eli anamuitana. Anathamanga kwa Eli. Koma Elia anati, 'Iai, sindidakuitana'. Samueli anabwerera ku bedi.
Mulungu anaitananso Samueli, 'Samueli! Samueli!' Samueli anaganiza, 'Kuyenera Eli kundiitana'. Koma pamene anathamanga kwa Eli, Eli anati, 'Iai, mwana wanga, sindidakuitana'. Ndipo Samueli anabwerera ku bedi.
Koma kenaka anamvanso Mau, 'Samueli! Samueli!'
Samueli anathamanganso kwa Eli. Nthawi iyi Eli anati, 'Tsono ndidziwa kuti wakuitana ndi yani. Ndi Ambuye! Bwerera ku bedi. Ndipo ngati umvanso mau ake, uyenera kunena, 'Nenani, Yehova, ndipo ine ndidzamva'.
Samueli anakhalanso pansi pa bedi. Sanakhoze kukhulupirira kuti Mulungu angalankhule kwa iye ndithu. Iye anali cabe mnyamata. Anakhazikika. Anamva. Ndipo kenaka anamvanso Mau, 'Samueli! Samueli!'
Ndipo iye anayankha, 'Nenani, Ambuye. Ndidzamva!'
Usiku womwewo Mulungu analankhula kwa Samueli. Anamuuza zimene zidzacitika.
Kucokera kwa nthawi iyo, Mulungu analankhula kwa Samueli nthawi zambiri. Samueli anasanduka m'modzi wa aneneri akulu. Anauza anthu zimene Mulungu anafuna iwo kucita.
Mulungu analankhula kwa anthu ena ambiri. Iwonso anali aneneri. Mulungu anawatuma kuuza mau ake kwa anthu ake.

**Kukambirana**
1. Chulani maina a anthu awiri amene Mulungu analankhula nao.
2. Kodi Mulungu analankhula bwanji kwa Samueli?
3. Kodi Samueli anaona Mulungu?
4. Kodi Samueli anayankha bwanji kuitanidwa kwake?
5. Kodi mumamva pamene Mulungu alankhula kwa inu m'Baibulo?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Tikuyamikani kuti munalankhula kwa anthu ambiri. Tikuyamikani kuti mulankhulanso nafe m'Baibulo. Tithandizeni kukhala omvera monga Samueli anakumverani. Tikupemphani m'dzina la Yesu Mpulumutsi weni-weni, Amen.

## 5. Mulungu alankhula kwa ife

*Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, Kuti ndisalakwire*
*Inu – Salimo 119.11*

**Kuwerenga**
1 Petro 1.24 ndi 25

**Malongosoledwe**
Tilankhula kwa Mulungu pamene timpempha. Titseka maso athu. Tiganizirako Mulungu. Ndipo kenaka tilankhula kwa Iye. Ndipo tidziwa kuti atimvera, pakuti atizungulira.
Koma Mulungu alankhula kwa ife kodi? Nanga tikhoza kumumvera?
Kale Iye analankhula kwa Samueli mnyamata. Analankhula kwa anthu ena ambiri. Koma amalankhula kwa inu ndi ine kodi?
Inde, alankhula kwa ife. Alankhula kwa ife m'njira zosiyanasiyana. Kopambana zonse, Iye alankhula kwa ife m'Buku lake.
Kale, pamene Mulungu analankhula kwa amuna, Iye anawauza kulemba mau ake. Anawauza kulemba mau ake m'buku. Iwo anapanga buku lalikulu. Timacha bukuli *Baibulo*. Baibulo ndi Mau a Mulungu.
Mulungu anasamalira ndi kusunga Baibulo. Baibulo linalembedwa zaka zambirimbiri zinapitazo, koma tikhoza kuliwerenga ngakhale lero. Mulungu anasamalira Baibulo pakuti Iye anafuna kulankhula kwa inu ndi ine mwa Baibulo.
Pamene tiwerenga Baibulo, Mulungu alankhula kwa ife. Pamene abusa atiwerengera Baibulo, Mulungu alankhula kwa ife. Pamene atate ndi amai atiwerengera Baibulo, Mulungu alankhula kwa ife. Pamene aziphunzitsi athu atiwerengera Baibulo ndi kutiuza nthano za m'Baibulo, Mulungu alankhula kwa ife.
Kuli mabuku ambirimbiri pa dziko lapansi. Baibulo ndi buku lodabwitsa kuposa mabuku onse. M'Baibulo lonse, Mulungu alankhula kwa ife.
Tikonda Baibulo popeza ndilo Mau a Mulungu.Tisamalira Baibulo lathu. Timawerenga Baibulo nthawi zambiri, pakuti tifuna kudziwa zimene Mulungu alankhula kwa ife.
Mulungu analankhula kwa ife m'njira yapadera kwambiri, pamene Iye anatuma Yesu Mwana wake kukhala pa dziko lapansi. Zinthu zambiri zimene Yesu ananena, zipezekanso m'Baibulo.
Ndipo Mulungu alankhula kwa ife pamene Mzimu wake alankhula mosamveka m'mitima yathu. Nthawi zina Mzimu alankhula mosamveka kutiuza kusacita mwano. Nthawi zina pamene tipemphera, Mzimu alankhula mosamveka kutiuza kuti Mulungu atimvera.
Ngakhale sitimvera mau a Mulungu mogwiritsa nchito makutu athu (monga Samueli anamva), Mulungu alankhula kwa ife. Alankhula kwa ife m'njira zambiri.

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu alankhula kwa ife m'njira yotani?
2. Cifukwa ciani Baibulo ndi buku lapadera kwambiri?
3. Cifukwa ciani kuphunzira mau a pa mtima ocokera m'Baibulo ndiko cinthu cabwino?
4. Cifukwa ciani tiyenera kufanizira zonse (ngakhale maloto, mau a anthu a Mulungu) ndi zimene zalembedwa m'Baibulo?
5. Kodi nchito yofunikira koposa ya abusa ndiyo ciani?

**Citsanzo ca pemphero**
Zikomo kwambiri, Mulungu wakumwambamwamba, kuti mufuna kulankhula nafe. Ndinu wolungama, woyera ndi wamkulu, komabe mufuna kuti tikudziwani. Dalitsani Baibulo kotero kuti Mau anu ndi monga mbeu yabwino yobala zipatso zabwino m'mitima ndi miyoyo yathu. Tikhululukireni kuti nthawi zambiri tikonda mau athu kuposa Mau anu. Tiphunzitseni kukumverani. Mwa Yesu Kristu tapempha izi, Amen.

## 6. Mulungu anatuma Mwana wace

Yesu ananena:
*Ine ndi Atate ndife amodzi – Yohane 10.30*

**Kuwerenga**
Yohane 14.8-10

**Malongosoledwe**
M'phunziro lotsiriza tinaphunzira momwe Mulungu adauza amuna kulemba buku: Baibulo. Mulungu anatipatsa Baibulo kuti tiphunzire za Iye ndi kumudziwa. Mulungu alankhula kwa ife mwa Baibulo. Ndi buku lapadera!
Koma Mulungu afuna ife kumudziwa bwino kwambiri. Afuna ife kumudziwa osati ngati Mulungu amene anatilenga cabe, komanso ngati Atate wa Kumwamba amene atikonda. Anatuma Yesu Mwana wake pansi pa dziko.
Pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi, angelo m'Mwamba anaimba cifukwa ca cisangalalo. M'modzi wa iwo anatsika pansi pa dziko lapansi kuuza abusa ena kuti angapeze Yesu Mwana wa Mulungu m'khola! Pa nthawi iyo Yesu anali mwana wa khanda. Kodi mudziwa kuti izo zinacitika pa tsiku liti?
Yesu anadza kwa anthu apadera a Mulungu, ndiwo Aisrayeli. Nthawi zambiri iwo achedwa Ayuda. Pamene Yesu anali wamsinkhu, Iye anayendera dziko lao. Anauza anthu za Mulungu ndi Ufumu wamkulu wa Mulungu. Anawauza kuti Mulungu atikonda. Paliponse pomwe Yesu anapita, Iye anacita zabwino. Anaciritsa anthu odwala. Anapenyetsa akhungu. Anapatsa cakudya kwa iwo akumva njala. Anali Bwenzi la iwo akumva cisoni cifukwa ca macimo ao.
Tsiku lina, pamene Yesu anali kulankhula ndi ophunzira ake za Atate wake wa Kumwamba, Filipo anati kwa Iye, 'Ambuye, tionetseni Atate'.
Yesu anati, 'Ndiri ndi inu nthawi yaikulu, Filipo; sunandidzindikire, si m'mene? Cabwino, ngati wandiona Ine, waona Atate!'
Kodi Yesu anatanthauza ciani?
Cabwino, Iye anatanthauza kuuza Filipo, komanso inu ndi ine, kuti Mulungu Atate wathu wa Kumwamba, ali cimodzimodzi monga Yesu, Mwana wake!
Inde, tidziwa kuti Yesu anali wabwino ndi wokoma mtima. Anacitanso zinthu zazikulu ndi zodabwitsa: kuciritsa odwala, kupenyetsa akhungu ndi ngakhale kuukitsa akufa nthawi zina! Pamene Yesu anacita nchito zotero, Iye anationetsa momwe Atate ali wabwino, wokoma mtima, wamkulu ndi wodabwitsa.
Nthano izi za Yesu zalembedwa m'Baibulo: m'mbali ya Cipangano Catsopano m'Baibulo. Ndiye, kuwerenga Baibulo ndi njira yabwino koposa kuphunzira za Mulungu. Tiphunzira za Iye mwa kuona zimene analenga: dziko lapansi, kumwamba ndi zina zonse zimene ziri pa dziko lapansi kapena m'thambo. Koma njira yabwino koposa kuphunzira kudziwa Mulungu ndiyo mwa kuwerenga buku lake, Baibulo. Iri litiuza zimene Iye analankhula kwa anthu a kale. Ndipo litiuza za zodabwitsa zonse zimene Yesu anacita. Iye anatifera!
Pamene tiganiza za cikondi cacikulu ca Yesu kwa ife, tiyenera kukumbukira kuti Mulungu Atate Kumwamba atikonda cimodzimodzi. Tingakhale otsimikiza kwa ici, pakuti Yesu ananena, 'Ine ndi Atate ndife amodzi' (Yohane 10.30).

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani Mulungu Atate anatuma Mwana wace pa dziko lapansi?
2. Fotokozani cifukwa ciani cikondi ca Mulungu ndi codabwitsa.
3. Kodi mumayankha bwanji cikondi ca Mulungu?
4. Kodi Yesu anaonetsa bwanji kuti afuna anthu ocimwa kulapa ndi kuwakhululukira macimo ao?
5. Citanthauzanji kuti Yesu ndi Atate ake ndiwo amodzi?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Atate, Tikuyamikani kuti munatuma Mwana wanu Yesu Kristu pa dziko lapansi. Cifukwa ca Iye tikhoza kudziwa Inu kuposa mwa cilengedwe cabe. Yesu anationetsa kuipa kwa uchimo komanso kuti tiloledwa kupita kwa Inu mwa Iye. Tiphunzitseni kusiya macimo kuti tikulondolani ndi mitima yathu onse. Tapempha izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.

**Sewero**
Pezani mau onse

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | C | H | I | T | O | L | B | L | K |
| M | I | T | I | M | A | L | N | M | U |
| R | L | R | E | Y | U | B | M | A | T |
| B | E | M | W | A | M | B | A | P | E |
| A | N | G | E | L | O | P | H | A | M |
| I | G | R | A | D | S | T | M | L | B |
| B | E | U | K | U | L | U | O | U | E |
| U | D | D | A | P | F | W | S | K | N |
| L | W | V | N | S | Z | Y | E | S | U |
| O | E | T | A | T | A | N | G | O | K |
| M | U | L | U | N | G | U | F | C | A |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| Mulungu | Yesu | Ambuye | mitima | kulapa |
| kutembenuka | angelo | Atate | nchito | cilengedwe |
| Baibulo | Mose | Mwamba | ukulu | ana |

**Sewero**
Lembani malembo pa malo ao

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 6 | 21 | 14 | 1 | 14 | 9 |
| | | | | | |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 25 | 5 | 8 | 15 | 22 | 1 |
| | | | | | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 | 16 | 15 |
| | | | | |

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 13 | 21 | 4 | 26 | 1 | 11 | 8 | 1 | 12 | 1 |
| | | | | | | | | | |

| | | |
|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 |
| | | |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 13 | 15 | 25 | 15 |
| | | | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 1 | 13 | 15 | 19 | 9 |
| | | | | |

5.6A

| | | | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 | 14 | 15 |
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M | N | O |

| | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
| P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.
Yeremiya 29.13

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com